4. Ife tikuganiza kuti Iye anaŵakonda. Phunziro limeneli likutithandiza kuti timvetsetse phunziro lathu lalero. Ife tikuphunzira za kubadwa kwa Yesu Khristu ku Betelehemu. Dzulo tinaphunzira kuti Khristu anali Mulungu. Lero tiphunzira kuti Iye anakhala munthu.

Mfumu ya mu nthano yathuyi inasiya nyumba yake yaikulu ndi kukakhala m'dziko lapansi. Iye anali kugawana nafe chimwemwe ndi zisoni zathu. Iye anali munthu ngati ife. Kodi Iyeyu anabwera bwanji? Iye anabadwa monga kamwana chimodzimodzi mmene inu ndi ine tinabadwira.

Ngati Mulungu anakhala munthu, kodi muli kuganiza kuti anali kufuna kuchitira anthu chiyani?

______________________________

==============================================================

5. Tidzakambirana za izi tonse pamodzi. Yesu anafuna kuchita zinthu zambiri. Monga mfumu ya m'nthano yathu, Yesu anafuna kuthandiza anthu. Iye anafuna kupulumutsa anthu kuchokera ku machimo awo. Koma kuti achite zimenezi Iye anayenera kukhala munthu. Mwana wa Mulungu yekha adayenera kukhala munthu. Chimenechi ndicho chinthu chokondweretsa kwambiri pa za kubadwa kwa Yesu.

Kodi ndi liti limene Mulungu anakhala munthu? ______________

______________________________________________

==============================================================

6. Mulungu anakhala munthu pamene Khristu anabadwa. Chimenechi ndicho chinthu chokondweretsa koposa pa za kubadwa kwa Yesu. Pa nthaŵi imeneyi panali zozizwitsa zambiri. Namwali wosadziŵa mwamuna anali ndi mwana. Angelo anaimba. Nyenyezi yapadera inaonekera. Anzeru akummaŵa anafika. Koma chinthu chokondweretsa ndi chodabwitsa kwambiri ndi chakuti Mulungu anakhala munthu. Kuyambira pachiyambi Khristu anali Mulungu. Pamene Yesu anabadwa ku Betelehemu, Khristu anakhala munthu.

Pamene Yesu Khristu anakhala m'dziko lapansi, kodi Iye anali Mulungu ndi munthu?

______________________________

==============================================================

7. Iye anali Mulungu ndi munthu. Khristu sanaleke kukhala Mulungu ngakhale Iye anakhala munthu. Iye anapitirizabe kukhala Mulungu. Koma Iye analinso munthu. Iye anali Mulungu ndi Munthu.

SABATA LOYAMBA: KUBADWA KWA KHRISTU
TSIKU LACHITATU: KUBADWA KWA YESU M'BETELEHEMU

1. Dzulo tinaphunzira za Khristu asanadze m'dziko lapansi lino.

Kodi Khristu anali kuti asanabwere m'dziko lapansi?________________

Kodi Iye anali yani? ____________________________________

==================================================================

2. Khristu asanabwere m'dziko lino lapansi anali kwa Mulungu. Ndipo anali Mulungu. Ngati mwalemba kuti Iye anali Mwana wa Mulungu, mwalondolanso. Kunena kuti Khristu ndi Mwana wa Mulungu kumatanthauza kuti Iye mwini ndi Mulungu.

Lero tiona mmene Khristu anabadwira ku Betelehemu. Tiphunzira zinthu ziŵiri:

(1) Chinthu chodabwitsa kwambiri za kubadwa kwa Yesu ndi chakuti Mulungu anakhala munthu.

(2) Mulungu anakhala munthu kuti atipulumutse kuchokera ku machimo athu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Luka 2:1 mpaka 7. Kodi Mariya anachita chiyani pamene anali ku Betelehemu?

____________________________________________________

==================================================================

3. Mariya anabala mwana wa mwamuna ku Betelehemu. Mwanayo anali Yesu.

Pa nthaŵi ina panali mfumu ya mphamvu. Iye anali kukhala paphiri lalitali ndipo anali wolemera kwambiri. Iye anali mfumu yabwino. Anali kufuna kumathandiza anthu ake. Koma anaganiza kuti, "Ine sindingathe kuŵathandiza anthuwo ngati sindiwadziŵa. Choyamba Ine ndiyenera kuŵadziŵa ndipo iwo ayenera kundidziŵanso ine. Iwo ayenera kudziŵanso kuti ndikufuna kuŵathandiza.

Mfumu inakhala ikuganiza zimenezi kwa masiku ambiri. Ndipo anaganizira za kusiya nyumba yake ya paphiri. Iyo inatsika pa phiripo ndi kupita kwa anthuwo kukakhala nawo. Iyo adayenera kukhala monga mmene anthuwo anali kukhalira. Iyo inali kumva zisoni ndi chimwemwe pamodzi nawo kuti potero akhoze kuŵadziŵa. Ndipo anthuwo akanamvetsetsa kuti iyo ikufuna kuwathandiza iwo.

Kodi mukuganizira kuti mfumu imeneyi inakonda anthu ake? ____________
==================================================================

Kodi ndi pakubadwa kwa yani pamene Mulungu anakhala munthu?

_______________________________________________________________

==============================================================

8. Mulungu anakhala munthu mwa Yesu. Iye anasanduka munthu pamene Yesu anabadwa. Chimenechi ndicho chodabwitsa cha kubadwa kwa Yesu. Zimenezi sizinaoneke ndi kale lonse. Ndi chinthu chimene sichidzachitikanso. Mulungu anakhala munthu.

Kodi ndi m'mudzi uti umene Mulungu anakhalira munthu? _______________

==============================================================

9. Chinthu chodabwitsachi chinachitikira m'Betelehemu. Betelehemu ndi mudzi waung'ono mu Israyeli. Mudziwu ulipo ndipo ulipo ngakhale tsopano lino. Akhristu ambiri ochokera ku maiko ambiri amakachezako chaka ndi chaka.

Kodi ndani anakhala munthu pamene Yesu anabadwa kwa Mariya?

_______________________________

==============================================================

10. Ku Betelehemu Mulungu anakhala munthu. Chimenechi ndi chinthu chodabwitsa pa za kubadwa kwa Yesu. Mwana wa Mulungu anali ndi Atate kuchokera pachiyambi. Iye mwini anali Mulungu. Koma Iye anasiya malo ake ndi Atate. Iye anabadwa monga kamwana pa dziko lapansi. Yesu Khristu anali Mulungu ndi munthu.

Kodi ndi muukhanda wa yani umene Mulungu anakhala munthu?____________

==============================================================

11. Mariya anali ndi khanda ku Betelehemu. Zodabwitsa zambiri zinaoneka. Koma chinthu chimodzi chimene chinakhala chodabwitsa koposa zina zonse.

Kodi chinthu chodabwitsa koposa pa za kubadwa kwa Khristu ndi chiyani?

______________________________________________________________

==========================================================================

12. Chinthu chodabwitsa kwambiri ndi chakuti Mulungu anakhala munthu. Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu anachita zimenezi? Ndi chifukwa chifukwa chiyani Mulungu anakhala munthu? Iye anachita zimenezi kuti atipulumutse ife kuchokera ku machimo athu. Buku Lopatulika limatiphunzitsa kuti anthu onse anachimwa.

Aroma 3:23:
Pakuti onse anachimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu.

Popeza tonse tinachimwa, kodi ndani ayenera kutipulumutsa kuuchimo

__________ __________ __________

==========================================================================

13. Tonsefe tifunika kukhala opulumutsidwa. Mulungu anakhala munthu kuti atipulumutse ku machimo athu. Ife sitingathe kudzipulumutsa tokha ayi. Sitingathe kupulumutsa anzathu. Kotero Mulungu anatsika yekha kuchokera kumwamba m'malo modzatipulumutsa m'machimo athu.

Kodi.chinthu chodabwitsa kwambiri pa za kubadwa kwa Yesu ndi chiyani?

__________________________________________________________________________

==========================================================================

14. Chinthu chodabwitsa kwambiri ndi chakuti Mulungu anakhala munthu. Anthu anasowa mpulumutsi. Mulungu anakhala munthu, kuti akhale Mpulumutsi wathu. Iye anachita zimenezi m'malo mofuna kutipulumutsa ku machimo athu.

Kodi chimatanthauza chiyani kukhala opulumutsidwa ku machimo? Taona kuti Buku Lopatulika limanena kuti mphotho ya uchimo ndi imfa.

Aroma 6:23:
Pakuti mphotho yake ya uchimo ndi imfa.

Kodi chidzaoneka ndi chiyani kwa anthu amene sanapulumutsidwe ku machimo?

________________________________________

===============================================================

15. Anthu amene sanapulumutsidwe machimo awo adzafa. Imeneyi siimfa ya thupi lokha. Zikutanthauza kuti mzimu wa munthu udzavutika munthuyo akadzafa. Iye adzasiyanitsidwa ndi Mulungu ku nthaŵi zonse. Chimenechi ndicho chilango cha tchimo. Koma Mulungu anakhala munthu kuti atipulumutse ife kuchokera ku chilango cha tchimo.

Mulungu anakhalanso munthu kuti atipulumutse ife kuuchimo. Ife tikhoza kukhululukidwa ndipo tikhoza kukhala osinthika. Yesu anadza kudzatipulumutsa ife kuchokera ku mphamvu ya uchimo. Ife sitiyenera kumachimwa. Tsopano tikhoza kumakhala abwino ndi moyo wa chiyero.

Ngati Yesu anatipulumutsa ife, kodi tiyenera kusiya chiyani?

________________________________________

===============================================================

16. Pamene tapulumutsidwa tiyenera kusiya machimo. Ife tinapulumutsidwa kuchokera ku chilango cha uchimo chimene chili imfa. Ife tinapulumutsidwanso ku machimo. Zinthu ziŵirizi ndi zimene tili kutanthauza tikamati tinapulumutsidwa kuchokera kuuchimo.

Kodi chinthu chodabwitsa kwambiri pa za kubadwa kwa Yesu Khristu ndi chiyani?

________________________________________

===============================================================

17. Chinthu chodabwitsa kwambiri ndi chakuti Mulungu anakhala munthu. Iye anachita zimenezi pamene Yesu Khristu anabadwa mwa Mariya.

Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu anakhala munthu? ________________

________________________________________

===============================================================

18. Mulungu anakhala munthu kuti atipulumutse kuchokera ku machimo. Munthu ameneyu ndi Yesu Khristu.

Kodi muli kuganiza kuti tiyenera kuchita chiyani poonetsa kuthokoza kwathu kwa Iye? ____________________

====================================================================

19. Tidzakambirana za yankho lanu m'kalasi.

Kodi chinthu chodabwitsa koposa pa za kubadwa kwa Yesu Khristu ndi chiyani? ____________________

____________________

Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu anachita zimenezi? ____________________

____________________

====================================================================

SABATA LOYAMBA: KUBADWA KWA KHRISTU
TSIKU LACHINAYI: MNGELO ACHEZERA MARIYA

1. Dzulo tinaphunzira za kubadwa kwa Yesu.

Kodi chinthu chodabwitsa kwambiri pa za kubadwa kwa Yesu ndi chiyani?

______________________________________________

Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu anachita zimenezi?

______________________________________________

================================================================

2. Chinthu chodabwitsa koposa ndi chakuti Mulungu anakhala munthu. Iye anachita zimenezi kuti atipulumutse ife ku machimo.

Pamene Yesu anabadwa panaoneka zinthu zambiri zodabwitsa. Angelo analankhula kwa abusa. Nyenyezi inatsogolera anthu anzeru. Yesu Khristu anali wosiyana ndi anthu ena onse. Iye anali Mulungu ndi munthu. Mulungu anagwiritsa ntchito njira yosiyana pakubadwa kwa Yesu Khristu. Chimenechi ndi chimene tikhale tikuphunzira lero.

(1) Kubadwa kwa Yesu kunali kosiyana chifukwa Iye anabadwa mwa mkazi amene anali osadziŵa mwamuna ndi kale lonse.

(2) Mariya namwaliyo anali ndi mwana wa mphamvu ya Mzimu Woyera.

Kubadwa kwa Yesu Khristu kunalengezedwa ndi mngelo. Kodi inu mungamve bwanji ngati mngelo atakuchezerani?

______________________

______________________________________________

================================================================

3. Mwina inu mukhoza kukhala okondwa. Kapena mukhoza kukhala ndi mantha. Buku Lopatulika linanena zambiri za angelo. Angelo safanana ndi ife. Iwo amachokera ku mwamba. Ife sitidziŵa mmene amaonekera, koma amakhala ndi Mulungu. Nthaŵi zina Mulungu amatumiza mngelo ku dziko lapansi. Ndipo mngeloyo amabwera ndi uthenga wochokera kwa Mulungu.

Pafupifupi zaka zikwi ziŵiri zapitazo kunali msungwana wosakwatiwa wotchedwa Mariya. Iye anali kukhala m'dziko la Israyeli. Iye anasankhidwa ndi Mulungu pa ntchito yapadera. Mulungu anatumiza mngelo

udzamuuza za zimenezi.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Uthenga wa Mulungu wopyolera mwa mngelo. Wêrengani Luka 1:26; mpaka 35. Kodi mngelo anamuuza Mariya kuti adzachita chiyani?

__________________________________________

______________________________________________________________________

==========================================================================

4. Mngelo anauza Mariya kuti adzabala mwana wa mwamuna. Umenewu unali uthenga wochokera kwa Mulungu. Ndipo mwanayo adzakhala Mwana wa Mulungu. Mariya anati kwa mngeloyo, "kodi chimenechi chidzatheka bwanji popeza ndilibe mwamuna?"

Inu mukudziŵa chifukwa chimene Mariya anafunsira funso limeneli. Mariya anali namwali. Namwali ndi mkazi wosakwatiwa. Mariya anali asanakhale malo amodzi ndi mwamuna wina aliyense. Komabe mngelo anamuuza kuti Mariya adzabala mwana wa mwamuna.

Kodi Mariya anali wokwatiwa? ____________________

==========================================================================

5. Mariya anali wosakwatiwa. Timadziŵa kuti mkazi ayenera kukhala malo amodzi ndi mwamuna kuti abale mwana. Njira imeneyi ndi imene Iye angakhalire ndi pathupi. Koma kubadwa kwa Yesu kunali kosiyana. Mayi wa Yesu anali wosakwatiwa. Iye anali namwali. Iye sanakhale malo amodzi ndi mwamuna aliyense. Tsopano tikumvetsetsa chifukwa chimene Mariya anafunsira kuti akhoza kukhala bwanji ndi mwana?

Kodi mkazi amene sanakhale malo amodzi ndi mwamuna timamutcha yani?

____________________________________________________________

==========================================================================

6. Mkazi amene sanagone malo amodzi ndi mwamuna amatchedwa namwali.

Kodi mayi wa Yesu anali yani? ___________________________________

Kodi anali wokwatiwa kapena anali namwali? __________________________

==========================================================================

7. Mariya anali namwali. Pamene mngelo anamuuza iye kuti adzakhala ndi mwana, nkuti asanakwatiwe. Patapita nthaŵi Yosefe anamutenga iye kukhala mkazi wake.

Mateyu 1:24-25:

> Ndipo Yosefe anauka tulo take, nachita monga anamuuza mngelo wa Ambuye, nadzitengera yekha mkazi wake; ndipo sanadziŵa iye kufikira atabala mwana wake.

Zimenezi zikutanthauza kuti Yosefe sanakhale naye malo amodzi ndi Mariya kufikira Yesu atabadwa.

Kodi Yosefe anali atate weniweni wa Yesu? ____________________

==================================================================

8. Yosefe sanali atate wa Yesu. Yosefe sanakhale malo amodzi ndi Mariya kufikira pamene Yesu anabadwa. Yesu anabadwa mwa namwali.

Kodi kubadwa kwa Yesu kunali kosiyana ndi kubadwa kwa anthu ena?

________________________________

Kodi Mariya anali munthu wotani pamene anabereka Yesu? ______________

==================================================================

9. Mariya anali namwali pamene anabala Yesu. Kubadwa kwa Yesu kunali kosiyana ndi anthu ena. Yesu mwina anali wosiyana ndi anthu ena. Iye anali munthu, koma analinso Mulungu.

Kodi kubadwa kwa Yesu kunali kosiyana bwanji ndi anthu ena?

__________________________________________________________________

__________________________________________________________________

==================================================================

10. Yesu anabadwa mwa namwali. Uku ndiko kusiyana kwa kubadwa kwake. Pamene mngelo anauza Mariya kuti adzabala mwana iye anafunsa kuti, "kodi zimenezi zidzatheka bwanji, popeza sindidziŵa mwamuna?" Taonani yankho la mngelo.

Luka 1:35:

Ndipo mngelo anayankha, nati, kwa iye, "Mzimu Woyera adzafika kwa iwe, ndi mphamvu ya wamkukukulu idzakuphimba iwe: chifukwa chakenso choyeracho chikadzabadwa, chidzatchedwa Mwana wa Mulungu."

Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi ndani amene adzafika kwa Mariya ndi kumupatsa mphamvu yobalira mwana?

______________________________

==========================================================================

11. Mngelo anauza Mariya kuti Mzimu Woyera adzafika kwa iye. Mphamvu ya Wamkulukulu idzamuphimba iye. Izi zikutanthauza kuti Mzimu Woyera ndiye amene anamupatsa mphamvu yoberekera mwana. Izi zinaphunzitsidwa m'buku la Mateyu.

Mateyu 1:18:

Ndipo kubadwa kwake kwa Yesu Khristu kunali kotere: Amayi wake Mariya anapalidwa ubwenzi ndi Yosefe koma asanakomane anapezeka iye ali ndi pakati mwa Mzimu Woyera.

Kodi Mariya adayenera kuchita chiyani mwa mphamvu ya Mzimu Woyera?

____________________________________________________________

==========================================================================

12. Mariya adayenera kukhala ndi mwana. Iye mkuti asanakwatiwe ndi Yosefe. Pamene Yosefe anamva kuti Mariya ali ndi pakati anakhumudwa. Mwana ameneyu sanali wake. Iye anaganiza kuti mwanayo ndi wa amuna ena

Mateyu 1:20:

Koma pakusinkhasinkha iye zinthu izi, onani mngelo wa Ambuye anaonekera kwa iye m'kulota, nanena "Yosefe, mwana wa Davide, usaope kudzitengera wekha Mariya mkazi wako; pakuti icho cholandiridwa mwa iye chili cha Mzimu Woyera."

Kodi ndani anapereka mphamvu kwa Mariya kuti akhale ndi mwana?

____________________________________

==========================================================================

13. Mzimu Woyera ndiye amene anapereka mphamvu zimenezi kwa Mariya. Yosefe anali munthu wabwino. Mulungu anamuuza kuti Mariya adzakhala ndi mwana. Mwanayo adzakhala mwana wa Mulungu. Pamene Yosefe anamva izi, sanakane kumukwatira iye. Iye anamutenga monga mkazi wake ndi kumakhala naye. Koma sanam'dziwa iye kufikira Yesu atabadwa.

Kodi kubadwa kwa Yesu ndi kubadwa kwa anthu ena kunali kosiyana bwanji?

____________________________________________________________

==========================================================================

14. Yesu anabadwa mwa namwali.

Kodi ndi mphamvu yanji imene Mariya namwaliyo anaonera mwana?

________________________________________

==========================================================================

15. Mariya anachita zimenezi ndi mphamvu ya Mzimu Woyera. Mulungu anafuna kuthandiza anthu. Iye anafuna kuŵapulumutsa. Iye akanakhoza kuchita zimenezi Iye mwini pakudzisandutsa munthu.

Kodi mukuganizira kuti ndikofunika kwa inu kuphunzitsa kuti Khristu anabadwa mwa namwali?

__________________________________

Chifukwa chiyani? _________________________________________

____________________________________________________________

==========================================================================

16. Tidzakambirana za izi m'kalasi.

Kodi kubadwa kwa Yesu kunali kosiyana motani ndi kubadwa kwa anthu ena?

____________________________________________________________

Kodi ndi mphamvu yanji imene Mariya namwaliyo anaonera mwana?

________________________________________

==========================================================================

SABATA LOYAMBA: KUBADWA KWA KHRISTU
TSIKU LACHISANU: MNGELO ANAUZA ABUSA

1. Dzulo tinaona kuti kubadwa kwa Yesu kunali kosiyana ndi anthu ena.

Kodi kubadwa kwa Yesu kunali kosiyana bwanji ndi kubadwa kwa anthu ena?

_______________________________________________

Kodi ndi mphamvu yotani imene Mariya namwaliyo anaonera mwana?

_______________________________

==========================================================

2. Yesu Khristu anabadwa mwa namwali. Mariya analandira mphamvu kuchokera kwa Mzimu Woyera kuti akhale ndi mwana. Yesu anali wosiyana ndi anthu onse. Iye anali munthu komanso anali Mulungu.

Kubadwa kwa Yesu Khristu kunali Uthenga Wabwino. Anthu oyamba kumva mbiri yabwinoyi anali abusa. Iwo anali kutali kuthengo ali kuyang'anira ziweto zawo pakati pa usiku.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Luka 2:8 mpaka 20. Masiku ano ngati mwana wofunika abadwa nkhaniyo imaulutsidwa pa wailesi kapenanso m'manyuzi pepala. Koma zimenezi sizinachitike motero ndi Yesu. Kodi abusa anadziŵa bwanji za kubadwa kwa Yesu?

_______________________________________________

==========================================================

3. Mngelo anauza abusa. Izi zimatisonyeza kuti kubadwa kwa Yesu kunali kofunika kwambiri. Mngelo anagwiritsa ntchito maina atatu polankhula za Khristu. Mainawo ali m'ndime iyi.

Luka 2:11:

> Pakuti wakubadwirani inu lero, m'mudzi wa Davide,
> Mpulumutsi amene ali Khristu Ambuye.

Maina atatuwa amatiuza ife mmene mwanayu aliri kufunika kwake. Kodi m'ndime imeneyi ndi maina ati amene anapatsidwa kwa Yesu?

(1) ______________ (2) ______________

(3) ______________

Yesu anapatsidwa maina atatu. Tiphunzira mainawo mphunziro lino. Tiphunziranso chifukwa chimene Yesu anapatsidwira maina amenewa. Naŵa mainawo ndi zifukwa zake. Awerengeni bwinobwino.

(1) Mpulumutsi - kuonetsa kuti Iye anadza kudzatipulumutsa.
(2) Khristu - kuonetsa kuti Iye anali mfumu yolonjezedwa.
(3) Ambuye - kuonetsa kuti Iye ndi Ambuye.

Kodi ndi dzina liti limene linapatsidwa kwa Yesu posonyeza kuti Iye anabwera kudzatipulumutsa ku machimo athu?

______________________

==========================================================================

5. Yesu anali kutchedwa Mpulumutsi. Dzina lakuti Yesu limatanthauza kuti Mpulumutsi. Tsiku lina mnyamata wotchedwa Yosefe anali kusamba mu mtsinje. Iye anamira padziŵe pakuya ndi kupita pansi pamadzi. Iye sanali kutha kusambira. Yosefe anamira, koma bwenzi lake Paulo anamutulutsa iye m'madzimo. Paulo anali mpulumutsi wa Yosefe.

Tsiku lina nyumba ya Petro inali kupysa. Ndipo ana a Petro anali mkati mwa nyumbayo kotero kuti sanathe kutuluka. Davide anathyola chitseko ndi kuŵatulutsira kunja anawo. Iye anali mpulumutsi wawo.

Kodi Mpulumutsi wathu wotichotsa kumachimo ndani? ________________

==========================================================================

6. Mpulumutsi wathu ndi Yesu. Si aliyense amene amagwa m'madzi akuya. Si aliyense amene ayenera kupulumutsidwa pamoto. Koma tonsefe tifunika mpulumutsi wa machimo athu. Buku Lopatulika limanena kuti onse anachimwa. Limanena kuti chilango cha tchimo ndi imfa. Imeneyi ndi imfa ya muyaya. Tiyenera kupulumutsidwa kuchokera ku machimo.

Kodi ndi chifukwa chiyani angelo anatcha Yesu kuti ndi Mpulumutsi?

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

==========================================================================

7. Izi zinaonetsa kuti Yesu anadza ku dziko lino lapansi kudzatipulumutsa. Iye anadza kudzatipulumutsa kuchokera ku machimo athu.

Kodi ndi dzina lotani limene mngelo anatchula Yesu posonyeza kuti Iye anadza kudzatipulumutsa?

_______________________________________

=====================================================================

8. Mngelo anatchula mwana Yesu ndi maina atatu. Dzina loyamba anali Mpulumutsi. Lembani chifukwa kapena cholinga cha dzina limeneli pa mzere woyambawo. Ndipo muwerenge maina enawo ndi zolinga zawo.

Yesu amatchedwa kuti:

(1) Mpulumutsi - ______________________________
(2) Khristu - kuonetsa kuti anali mfumu yolonjezedwa.
(3) Ambuye - kuonetsa kuti Iye ndi Mulungu.

=====================================================================

9. Iye anatchedwa Mpulumutsi kuonetsa kuti Iye anadza kudzatipulumutsa ife. Iye anatchedwanso Khristu. Iye anapatsidwa dzina limeneli kuonetsa kuti Iye anali mfumu yolonjezedwayo.

M'Chipangano Chakale munali lonjezano lakuti mfumu ya Aisraeli idzabwera. Iye adzakhala mfumu ya mphamvu. Iye adzakhala wabwino koposa mafumu ena onse. Nthaŵi zonse mfumu inali kuthiridwa mafuta pamutu posonyeza kuti ndi wosankhidwa ndi Mulungu. Liu lakuti "Khristu limatanthauza za wina wake amene anathiridwa mafuta pamutu pake. Mwina mukhoza kudziŵa liu lina lakuti "Mesiya." Khristu ndi Mesiya limatanthauza chinthu chimodzimodzi. Iwo ndi mawu amodzi wochokera m'zilankhulo zosiyana.

Kodi ndani amene anali kutchedwa Khristu kapena Mesiya posonyeza kuti Iye anali mfumu yolonjezedwayo?

_______________________________________

=====================================================================

10. Yesu anali kutchedwa Khristu. M'nthaŵi ya Chipangano Chakale nthaŵi zonse Mulungu anali kusankha mafumu. Iye anali kusankhanso ansembe ndi aneneri.

Aneneri a m'Chipangano Chakale anali kunena za munthu wina amene adzabwera. Iye adzakhala mfumu yaikulu. Iye adzakhalanso wansembe wamkulu ndi m'neneri. Kukhala mfumu, wansembe ndi m'neneri, ayenera kusankhidwa ndi Mulungu. Aneneri analonjeza kuti mfumu yosankhidwa ndi Mulungu idzabwera.

Pamene mngelo anamutcha "Khristu" mwanayo kodi zimenezi zinali kuonatsa chiyani?

______________________________________________

==========================================================================

11. Izi zinasonyeza kuti Iye anali mfumu yolonjezedwayo. Zinasonyeza kuti Iye anali wosankhidwa ndi Mulungu. Dzina lakuti "Mesiya" limatanthauza munthu amene anasankhidwa ndi Mulungu. Izi zimasonyeza kuti Iye ndi mfumu yolonjezedwayo. Koma mngelo sanagwiritse ntchito liu lina limene limatanthauza chinthu chimodzimodzi chomwecho ayi.

Kodi ndi dzina lotani limene mngelo anapatsa Yesu posonyeza kuti Iye anali mfumu yolonjezedwayo?

______________________________

==========================================================================

12. Mngelo anamutcha Iye "Khristu," pamene Yesu anabadwa. Ayuda anali kudikira mfumu yolonjezedwa. Abusa anamva mngelo akutchula khanda "Khristu." Ndipo iwo anadziŵa kuti pali kanthu kena kapadera.

Pambali poonetsa kuti Iye anali wosankhidwa, kodi dzina lakuti "Khristu limaonetsa chiyani za Yesu?

______________________________

==========================================================================

13. Izi zinaonetsa kuti Iye anali mfumu yolonjezedwa. Pamene abusa anamva kuti Khristu wabadwa, iwo anadziŵa kuti wolonjezedwa wafika. Anadziŵa kuti khandalo linali Mesiya wolonjezedwa. Mulungu kupyolera mwa aneneri analonjeza kuti Mesiya adzabwera. Tsopano anadziŵa kuti wabadwa.

Kodi ndani anatchulidwa ndi mngelo kuti ndi Khristu posonyeza kuti Iye anali mfumu yolonjezedwayo?

______________________________

==========================================================================

14. Yesu anatchulidwa kuti ndi Khristu. Ayuda anali ndi lonjezano la m'Chipangano Chakale. Mwa Yesu, ulosi wa m'Chipangano Chakale unakwaniritsidwa.

Mngelo anapatsa Yesu maina atatu. Lembani chifukwa chimene mngelo anaperekera mainaŵa kwa Yesu.

(1) Mpulumutsi - ____________________

(2) Khristu - ____________________

(3) Ambuye - ____________________

==========================================================================

15. Yesu anali kutchedwa Khristu kuonetsa kuti Iye mabwera kudzatipulumutsa ife. Iye anali kutchedwa Khristu posonyeza kuti Iye anali mfumu yolonjezedwayo. Iye anapatsidwanso dzina lakuti Ambuye. Liu lakuti "Ambuye limapezeka mazana mazana m'Buku Lopatulika.

Genesis 12:1:
Ndipo Yehova anati kwa Abrahamu, "Tuluka iwe m'dziko lako, ndi kwa abale ako, ndi kunyumba ya atate wako, kunka kudziko limene ndidzakusonyeza iwe."

Masalmo 24:1:
Dziko lapansi nla Yehova ndi zodzala zake zomwe, dziko lokhalamo anthu ndi iwo okhala m'mwemo.

Mateyu 1:24:
Ndipo Yosefe anauka tulo take, nachita monga anamuuza mngelo wa Ambuye.

Kodi liu lakuti "Ambuye likunena za yani m'ndime zimenezi?

____________________

==========================================================================

16. Liwu lakuti "Ambuye" pamenepa likutanthauza Mulungu. Ndime zimenezi zili kulankhula za Mulungu. Mphunziro lathu sabata ino taona kuti Khristu ndiye Mulungu. Taonanso kuti anali wamoyo kuyambira pa chiyambi. Ife taona kuti Iye anali wamoyo monga mwana wa Mulungu.

Kodi ndi dzina liti limene mngelo anapatsa Yesu lomwe limaonetsa kuti Iye anali Mulungu? ____________________

==========================================================================

17. Iye anamutcha Ambuye. Taonaninso ndime iyi.

Luka 2:11:
Pakuti wakubadwirani inu lero, m'mudzi wa Davide, Mpulumutsi, amene ali Khristu Ambuye.

Kodi ndi chifukwa chiyani mngelo anatcha Yesu kuti ndi Ambuye?

____________________________________________________________

==========================================================================

18. Mngelo anamutcha kuti Ambuye posonyeza kuti Iye ndi Mulungu. Kumbukirani kuti Yesu anali Mulungu ndi munthu. Chimenechi chikutikumbutsa za phunziro lomwe taliphunzira kumayambiriro a sabata ino.

Kodi chinthu chodabwitsa koposa cha za kubadwa kwa Khristu ndi chiyani?

____________________________________________________________

==========================================================================

19. Chinthu chodabwitsa kwambiri ndi chakuti Mulungu anakhala munthu.

Lembani chifukwa chimene mngelo anapatsira maina aŵa kwa Yesu.

(1) Mpulumutsi - ________________________________________

(2) Khristu - ________________________________________

(3) Ambuye - ________________________________________

==========================================================================

SABATA LACHIWIRI: UKHANDA WA KHRISTU
TSIKU LOYAMBA: KUCHEZA KWA ANZERU AKUMMAWA

1. Kubadwa kwa Yesu kunali chinthu chachikulu kwambiri. Koma ndi anthu ochepa okha pa nthaŵi imeneyo amene.anadziŵa zimenezi. Poyamba mngelo anauza mbiri yabwinoyi kwa abusa.

Lembani chifukwa chimene mngelo anaperekera maina aŵa kwa Yesu.

(1) Mpulumutsi - ______________________________

(2) Khristu - ______________________________

(3) Ambuye - ______________________________

==========================================================================

2. Yesu anatchedwa Mpulumutsi posonyeza kuti Iye anabwera kudzatipulumutsa ife. Iye anatchedwa Khristu kuonetsa kuti Iye anali Mfumu yolonjezedwayo. Iye anatchedwa Ambuye kuonetsa kuti Iye anali Mulungu
Abusa anapita kukaona ndi kukapembedza Yesu. Iwo analemekeza Mulungu. Patapita nthaŵi ena anabwera kudzachezera Yesu. Ameneŵa anali anthu a nzeru aku mmaŵa. Iwo anabweretsa mphatso kwa Yesu. Lero tiphunzira za kupereka mphatso kwa Yesu.

(1) Mmalo mwa golidi wa Mfumu tikhoza kupereka kumvera.
(2) Mmalo mwa libano wa Mulungu tikhoza kupereka mapembedzo.
(3) Mmalo mwa mure wa Mpulumutsi wofera tikhoza kupereka mayamiko.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga pa Mateyu 2:1 mpaka 12. Kodi ndi anthu ati amene anadzachezera Yesu pa ndime zimenezi?

______________________________________________

==========================================================================

3. Anthu anzeru anabwera kudzaona Yesu. Anthu enanso anabwera kudzaona Yesu. Pamene Yesu anali ndi masiku makumi nayi (40) amoyo wake. Yosefe ndi Mariya anapita naye ku Yerusalemu. Iwo anapita naye ku Kachisi ndi kukamupereka kwa Mulungu monga momwe lamulo linanenera. Pamene iwo anali mkachisimo aneneri aŵiri anaona Yesu ndipo analankhula mawu amphamvu onena za Iye.
Ndipo Mariya ndi Yosefe anabwerera ndi Yesu ku Betelehemu. Anzeru akummaŵa anabwera kudzamuchezera. Odzachezaŵa anali kuchokera kutali ku maiko aku mmaŵa. Izi zinali zinthu zodabwitsa. Ku Israyeli kunali anthu ambiri. Koma Mulungu anatsogolera anthu anzeru kuchokera kutali

kuti adzaone mwana wake.

Kodi anzeru akummaŵa anabweretsa chiyani kwa Yesu ________________

==========================================================================

4. Anzeru akummaŵa anabweretsa mphatso. Iwo anali kukhala maiko aku mmaŵa kwa Israeli. Maiko awo akhoza kukhala Babuloni kapena Mediya kapena arabiya. Ife sitidziŵa bwino. Anthu ameneŵa anali kuphunzira za nyenyezi. Tsiku lina iwo anaona nyenyezi yowala kwambiri. Iwo anadziŵa kuti chinali chizindikiro chochokera kwa Mulungu. Iwo anapita kukapeza Mfumu ya Ayuda. Potsiriza nyenyezi inaŵatsogolera pamene anali Yesu.

Mateyu 2:11:

> Ndipo anagwa pansi nam'gwadira Iye; namasula chuma chawo, nampatsa Iye mitulo, ndiyo golidi ndi libano ndi mure.

Golidi ndi mphatso za mfumu. Kodi anzeru akummaŵa anali kufunafuna munthu wotani?

________________________________

==========================================================================

5. Anthu anzeru anali kuyang'ana mfumu. Iwo anali kufunafuna mfumu ya Ayuda. Pamene anapeza Yesu iwo anamupatsa golidi. Pa nthaŵi imeneyo golidi inali mphatso za mafumu. Korona wa mfumu anali wopangidwa ndi golidi. Mbale za mfumu zinali zopangidwa ndi golidi. Ndalama ya mfumu inali ya golidi.

Kodi mphatso ya golidi yochokera kwa anzeru akummaŵa inaonetsa chiyani za Yesu?

________________________________

==========================================================================

6. Mphatso ya anthu anzeru inaonetsa kuti Yesu anali mfumu. Yesu ndi mfumube kufikira tsopano. Iye si mfumu ya Ayuda okha. Iye ndi mfumu ya anthu onse. Yesu anadza kudzalalikira ndi kuphunzitsa za ufumu wa Mulungu. Iye ndi Mfumu ya ufumu umenewo. Yesu ndi wamphamvu koposa mfumu za maiko a dziko lapansi. Iye ndi mfumu ya mafumu.

Kodi ndi mphatso ya anthu anzeru iti imene idaonetsa kuti Yesu ndi mfumu?

____________________________________________

==================================================================

7. Anzeru akummaŵa anapereka golidi kwa Yesu. Iwo anadziŵa kuti Iye ndi mfumu. M' dziko lathu tili ndi mafumu ambiri. Nthaŵi zina amatchulidwa ndi maina ena. Iwo akhoza kutchulidwa kuti ndi ma Prime Ministers kapena kuti Head of State, kapenanso kuti Presidents. Komabe kaya amatchulidwa dzina lotani, iwo amalamulira anthu. Anthu amayenera kuwamvera iwo. Iwo ayenera kuonetsa kumvera kwa mfumu yawo.

Yesu ndiye mfumu yathu, kodi ife tiyenera kumupatsa chiyani mmalo mwa golidi?

____________________________________________

==================================================================

8. Tiyenera kumumvera Iye. Yesu ndi mfumu ya mafumu. Ngati ife tili Akhristu, Yesu ndi mfumu yathu. Popeza Iye ndi mfumu yathu, tiyenera kumumvera Iye.

Pamene tikumumvera Iye timaonetsa kuti Yesu ndi mfumu yathu. Kodi ndi ndani anapereka golidi kuonetsa kuti Yesu ndi mfumu?

____________________________________________

==================================================================

9. Anthu anzeru anapereka golidi kwa Yesu. Chimenechi chinaonetsa kuti Iye anali mfumu. Komanso pali kanthu kena kamene anthu amapereka kwa mfumu yawo. Iwo amamvera.

Mphatso za anzeru akummaŵa zimatikumbutsa ife kuti tizipereka kwa Yesu.
(1) Mmalo mwa golidi wa mfumu, kodi tikhoza kupereka chiyani?
(2) Mmalo mwa libano wa Mulungu tikhoza kupereka chipembedzo.
(3) Mmalo mwa mure wa Mpulumutsi wofera tikhoza kupereka chithokozo.

==================================================================